SABATA LACHISANU NDI CHIŴIRI: CHIPHUNZITSO CHA YESU CHA PAPHIRI
TSIKU LACHINAYI: KUKONDA NDI KUPEMPHERERA ADANI AKO

1. Taona kuti pa ulaliki umodzi wapa phiri, Yesu anaphunzitsa zinthu zambiri. Iye anaphunzitsa kuti ife timadalitsidwa tikaona zosoŵa zathu. Iye anaphunzitsa kuti ndife mchere ndi kuunika kwa dziko lapansi. Iye anaphunzitsa kuti zomwe timachita kwa anthu ena ndi zofunika kwambiri.

Ngati inu mutabwera kudzapembedza Mulungu ndi kukumbukira kuti mbale wanu ali nacho chifukwa cha pa inu, kodi mungachite chiyani?

Ngati mutayang'ana kwa mkazi ndi kumufuna iye m'njira yoipa, kodi Yesu anati tiri kuchita chiyani?

==========================================================

2. Ngati mwabwera kudzapembedza ndi kukumbukira kuti mbale wanu ali ndi mkwiyo pa inu, pitani mukapange mtendere pakati pa inu ndi iye. Ngati inu muyang'ana kwa mkazi ndi kumufuna iye m'njira yoipa, Yesu anati muli kuchita chigololo. Yesu anali ndi zinthu zambiri zophunzitsa mmene tingamakhalire.

(1) Pa Mateyu 5, Yesu anati sitiyenera kumalumbira mmalo mofuna kupanga anthu kuti akhulupirire zimene tiri kunena.

(2) Mmalo mofuna kubwezera choipa kwa adani athu, Yesu anati tiyenera kuwakonda ndi kuŵapempherera iwo.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuŵerenga Mateyu 5:33: kufika ndime 37. Ganizirani za njira imene anthu amalankhulira. Koma mumaganiza kuti anthu amalumbira chifukwa chiyani?

==========================================================

3. Pali zifukwa zambiri. Ena amalumbira kulimbikitsa mawu awo. Ena amalumbira kuti aopse anthu. Ena amalumbira pofuna kuti anthu aŵakhulupirire. Taonaninso zomwe Yesu ananena.

Mateyu 5:33-34:

> Ndiponso, munamva kuti kunanenedwa kwa iwo akale, Usalumbire konama, koma udzipereka kwa Ambuye zolumbira zako; koma Ine ndinena kwa inu, musamalumbire konse.

Kodi Yesu ali kuganiza kuti lamulo lakale la za kulumbira linali losakwana?

______________________________________________

==========================================================================

4. Yesu sanaganize kuti ndi chosakwanira. Lamulo lakale linati, "Musalumbire monama." Yesu anabwera kudzakwaniritsa lamulo. Iye anabwera kudzaphunzitsa njira yopamwamba yakakhalidwe ka moyo. Iye anabwera kudzatipatsa mphamvu yokhalira njira ya moyo imene Mulungu amafuna. Yesu anati ife sitiyenera kulumbira konse. Sitiyenera kufuna kuti tilumbire Ngati mawu athu ali woona, sitiyenera kufuna kuŵalimbikitsa. Ngati timasunga mawu athu nthaŵi zonse, sitiyenera kupanga anthu kuti atikhulupirire ife.

Kodi ndi anthu ati amene sayenera kulumbira konse? ________________

==========================================================================

5. Akhristu sayenera kuchita zimenezi. Nthaŵi zonse Akhristu ayenera kulankhula choonadi. Iwo nthaŵi zonse ayenera kusunga malonjezo awo. Iwo ayenera kukhala kotero kuti pamene iwo ali kulankhula, anthu ena azidziŵa kuti mawu awo ali woonadi.

Mateyu 5:37:

> Koma manenedwe anu akhale, inde, iyai, iyai; ndipo choonjezedwa pa izo chichokera kwa woipayo.

Kodi Yesu ananena kuti sitiyenera kuchita chiyani mmalo mofuna kupanga anthu kuti akhulupirire zomwe tikunena?

________________________

______________________________________________________

==========================================================================

6. Sitiyenera kulumbira. Koma ife timayesedwa kumachita monga momwe ánthu otizungulira amachitira. Nthaŵi zina timva anthu ali kunena kuti,

"Ngati chimenechi sichoona, mlongo wanga adzuke kumanda." Kapena "Ngati zimenezi sizili chomwechi ndikhoza kukakhala malo amodzi ndi mlongo wanga." Kapena kuti "Ndikulumbira Mulungu, zimenezi ndi zoonadi."

Mateyu 5:34-36:

> Koma Ine ndinena kwa inu, musalumbire konse, kapena kutchula kumwamba, chifukwa kuli chimpando cha Mulungu; kapena kutchula dziko lapansi, chifukwa lili popondapo mapazi ake; kapena kutchula Yerusalemu, chifukwa kuli mzinda wa Mfumu yaikulukulu. Kapena usalumbire kumutu wako, chifukwa sungathe kuliyeretsa mbu kapena kulidetsa bii tsitsi limodzi.

Kodi ife tili ndi mphamvu yoposa Mulungu, dziko lapansi, kapena mutu wathu womwe?

__________________________________________________

===========================================================================

7. Ife tilibe mphamvu yoposa zinthu zimenezi. Zimenezi sizathu. Zinthu zonsezi ndi za Mulungu. Sizoti tizizigwiritsa ntchito m'chifuniro chathu monga tifunira. Sitingathe kuzigwiritsa ntchito kuti tilimbikitse mawu athu.

Kodi Yesu ananena kuti sitiyenera kuchita chiyani kuti tipange anthu kukhulupirira mawu athu?

________________________________________

_______________________________________________________________________

===========================================================================

8. Sitiyenera kulumbira. Ife Akhristu timayenera kukhala osiyana. Pali njira inanso imene timayenera kukhala osiyananira. Yesu anauza akuphunzira, ake pa chiphunzitso chake cha pa phiri.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 5:38-48. Kodi anthu amene sali Akhristu amachita chiyani kwa adani awo?

_______________________________________________________________________

===========================================================================

9. Iwo amada adani awo. Iwo amaŵabwezeranso choipa chawo. Iwo amayesa kuŵapha. Iwo amaopanso adani awo ndi kumaŵathaŵa.

Ndi chinthu chapatali kukhala ndi mdani. Iye mwina akhoza kumafuna kukupha iwe. Ndi chinthu chapafupi kuda mdani wako. Koma Akhristu amayenera kuchitira adani zinthu ziŵiri.

(1) Kuŵakonda iwo
(2) Kuŵapempherera iwo

Kodi ndi ndani anaphunzitsa kuti timayenera kukonda adani athu ndi kuŵapempherera iwo?

____________________________________________

==================================================================

10. Yesu anaphunzitsa za chimenechi. Iye anaphunzitsa njira ya kakhalidwe ka moyo wopambana.

Mateyu 5:38-39:

> Munamva kuti kunanenedwa, Diso kulipa diso, ndi dzino kulipa dzino: koma ndinena kwa inu, musakanize munthu woipa; koma amene adzakupanda iwe pa tsaya lako lamamja, umtembenuzire linanso.

Ameneŵa ndi mawu ovuta kwambiri. Kodi ndi anthu ati amene amayenera kutembenuza tsaya lina ndi kukonda ndi kupempherera adani awo?

____________________________________________

==================================================================

11. Akhristu amayenera kuchita zimenezi. Chimenechi chimatanthauza ife. Nthaŵi zina ife timakhala ndi adani. Kutembenuza tsaya lina sikumatanthauza kuti ife tizidzipereka tokha kwa iwo. Chimatanthauza kuti ife sitiyenera kuchita motsutsana nawo. Bulusi anali ndi mdani. Usiku wina mdani uja anakhala wokwiya kwambiri ndipo anati adzapha Bulusi. Abwenzi a Bulusi anamuchenjeza kuti atenge banja lake ndi kupita kukakhala kwina. Bulusi anachita zimenezi. Bulusi anayesedwa kuti ade mdani ameneyu.

Kuchokera pa ndime imeneyi, kodi chinthu choyamba chimene timayenera kuchitira adani athu ndi chotani?

(1) ______________________ (2) Kuŵapempherera iwo.

==================================================================

12. Poyamba timayenera kuŵakonda iwo ndipo tiŵapempherere. Chimenechi sichinthu chapafupi. Ife sitingathe kuchita zimenezi mwa ife tokha. Timayenera kukhala ndi thandizo la Mulungu.

Mateyu 5:46-47:

> Chifukwa kuti ngati muŵakonda akukondana ndi inu mphotho yanji muli nayo? Kodi angakhale amisonkho sachita chomwecho? Ndipo ngati mulankhula (kapena kumvana) abale anu okhaokha, muchitanji choposa ena?

Kodi angakhale anthu akunja sachita chomwecho?

______________________________________________

==========================================================================

13. Ife timayenera kukonda adani athu. Ife tisoŵa thandizo lochitira zimenezi. Tikhoza kuŵakonda ndi thandizo lochokera kwa Mulungu. Ife tikhoza kusamalira za iwo. Tikhoza kuyesa kuŵathandiza iwo. Mwina iwo sangafune kutimvera ife. Mwina sangafune kukondedwa. Akhoza mwina kumangotitsutsa kwambiri ndi mochititsa manyazi.

Kodi ife tikhoza kupeza thandizo kuti lochitira chinthu chovuta choterechi chokonda adani athu?

______________________________________________

==========================================================================

14. Ife tikhoza kupempha Yesu kuti atithandize ife. Iye ndi amene anatipatsa lamulo limeneli. Iye adzagwira ntchito mwa ife. Ena amapemphera ndi kufunsa Mulungu kuti aononge adani awo. Chimenechi sichimene Yesu anaphunzitsa. Iye anati tiyenera kumapemphera, koma tiyenera kumaŵapempherera adani athu zinthu zabwino.

Ife timayenera kupempherera adani athu, kodi tiyenera kuŵachitira chiyani?

______________________________________________

==========================================================================

15. Tiyenera kukonda adani athu. Tikamachita zimenezi chidzakhala chinthu chodabwitsa kwambiri kwa anthu. Anthu adziko amada adani awo. Iwo amayesa kupeza njira zomenyana nawo.

Kuchokera pa ndime imeneyi, pamene tili kukonda adani athu, kodi tingatani kuti tiŵathandize iwo?

________________

================================================================

16. Ife tikhoza kuŵapempherera iwo. Chimenechi poyamba chimakhala chovuta. Koma Mulungu adzatithandiza ife. Iye amafuna kuti ife tikhale monga Iye mwini. Yesu amafuna kuti ife tikhale achilungamo.

Mateyu 5:45:

> Kotero kuti mukakhala ana a Atate wanu wakumwamba; chifukwa Iye amakwezera dzuŵa lake pa oipa ndi abwino namavumbwitsira mvula pa olungama ndi osalungama.

Kodi ndi ndaninso amene timayenera kuŵapempherera poonjezera abwenzi ndi abale athu?

________________

Kodi Yesu anati sitiyenera kuchita chiyani kuti anthu akhulupirire mawu athu?

________________

================================================================

17. Sitimayenera kulumbira. Timayenera kuchitira adani athu zinthu zomwe ife tingachitire abwenzi ndi abale athu. Mkhristu wina ku Zaire anatengedwa ndi adani ake. Iwo ananena kuti amulasa ndi mpholopolo. Koma iye poyamba anapempha kuti achite chinthu chimodzi. Iye anati, "Chovala changachi ndi chatsopano. Poyamba ndiyambe ndachivula chisanachite magazi. Ndipo mukhoza kutenga ndi kuchigwiritsa ntchito." Ndi Mulungu yekha amene angatipatse ife mphamvu yochitira zimenezi kwa adani athu.

Mmalo mobwezera zoipa kwa adani athu, kodi Yesu anati tiyenera kuchita chiyani kwa iwo?

(1) ________________ (2) ________________

================================================================

18. Tiyenera kukonda adani athu ndi kuŵapempherera iwo. Chikondi ndi cha mphamvu ndi chabwino. Chimamanga miyoyo. Chimakokera anthu kwa Khristu. Chidaninso ndi champhamvu, koma chimapha. Chimapha mdani

ndipo chimapha amene amadana ndi adani ake. Mulungu amafuna kuti tikhale monga Iye.

Mateyu 5:48:

> Chifukwa chake inu mukhale angwiro, monga Atate wanu wa kumwamba ali wangwiro.

Lembani chinthu chimodzi chomwe mungachitire adani anu sabata ino pofuna kumvera phunziro ili. Musalembe mawu akuti "kuwakonda." Nenani zimene mungachite.

______________________________________________

================================================================

19. Tidzakambirana za zimenezi tonse pamodzi.

Pa Mateyu 5, kodi Yesu anati ife sitiyenera kuchita chiyani kuti tipange anthu akhulupirire mawu athu?

______________________________________

Mmalo mofuna kubwezera zoipa kwa adani athu, kodi Yesu anati tiyenera kuŵachitira chiyani?

(1) ________________________ (2) ______________________

================================================================

TSIKU LACHISANU: TIYENERA KUPEMPHERA MWA M'TSERI NDI KUKHULULUKIRA

1. Taona kuti Akhristu enieni amakhala osiyana ndi anthu ena. Yesu anali kuphunzitsa ophunzira ake mmene iwo angakhalire. Iye anali kuwakonza kuti akagwire ntchito yake. Anthu ayenera kuona kuti miyoyo yawo ndi yosinthika.

Pa Mateyu 5, kodi Yesu anati tiyenera kuchita chiyani chimene chingapangitse anthu kumvera mawu athu?

______________________________

Mmalo mobwezera choipa kwa adani athu, kodi Yesu anati tiyenera kuchita chiyani?

(1) ____________________ (2) ____________________

==================================================================

2. Yesu anati sitiyenera kulumbira pofuna kuti anthu atikhulupirire. Iye anati, mmalo mobwezera choipa kwa adani athu, tiyenera kuwakonda ndi kuwapempherera. Izi zinali zinthu zodabwitsa kuti Yesu aphunzitse chifukwa Afarisi anali ndi malamulo awo. Iwo anali kuyesetsa kukhala olungama mwa kusunga malamulo. Iwo anali kuyesetsa kukhala abwino pakupereka chopereka ndi kupemphera patsogolo pa anthu. Ndipo Yesu anapereka chiphunzitso chatsopano.

(1) Kuchokera pa Mateyu 6, Mulungu adzapatsa mphotho kwa wopereka, wopemphera ndi kusala ngati achita mwa chisinsi.

(2) Ngati sitikhululukira anthu ena amene atichimwira, Mulungu sadzatikhululukira.

Tengani Buku Lopatulika tsopano ndipo muwerenge kwambiri za chiphunzitso cha pa phiri. Werengani Mateyu 6:1 mpaka 7. Werenganinso ndime 5. Ngati mapemphero a anthu aonekeratu pamaso pa anthu ena, kodi anthuwo alandiriratu chiyani?

______________________________

==================================================================

3. Iwo alandiriratu mphotho. Mphotho imeneyi ndi ya chiyamiko yochokera kwa anthu amene akuona ntchitozo. Koma mphotho yabwino imene tingathe kulandira ilipo.

Mateyu 6:1:

Yang'anirani kuti musachite zolungama zanu pamaso pa anthu kuti muonekere kwa iwo; pakuti ngati mutero mulibe mphotho ndi Atate wanu wa kumwamba.

Kodi ndani adzapereke mphotho kwa iwo opemphera ndi kukhululukira mwa m'tseri? ______

==========================================================

4. Atate wathu wa kumwamba adzaŵapatsa mphotho. Iye adzaŵapatsa madalitso ake. Mulungu safuna kuti tichite zinthu pofuna kuti anthu atiyamikire ayi. Iye safuna kuti tizikhala onyada ndi zimene timachita.

Mateyu 6:2:

Chifukwa chake pamene paliponse upatsa mphatso zachifundo, usamaomba lipenga patsogolo pako, monga amachita onyenga m'masunagoge, ndi m'makwalala, kotero kuti atamandidwe ndi anthu.

Anthu ambiri mumpingo amafuna kuti anthu ena aziona zopereka zimene iwo amapereka. Iwo amapemphera pemphero lalitali monga ulaliki. Kodi Mulungu akhoza kupereka mphotho pa zimenezi? ______

==========================================================

5. Mulungu sangapereke mphotho pa zinthu zimenezi. Anthu amene amapereka zopereka zawo pamaso pa anthu amalandiriratu mphotho zawo. Anthu amene amapemphera mapemphero a akuluakulu amalandiriratu mphotho pamene anthu akumva. Ndipo zopereka zimenezi Mulungu sazidalitsa. Mapemphero oterowo Mulungu sayankha.

Mateyu 6:3-4:

Koma iwe popatsa mphatso zachifundo, dzanja lako lamanzere lisadziŵe chimene lichita dzanja lako lamanja; kotero kuti mphatso zako zachifundo zikhale za m'tseri; ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe.

Kodi ndi kupereka kotani kumene Mulungu amadalitsa? ______

______

==========================================================

6. Kupereka mwa m'tseri Mulungu amakudalitsa. Kupemphera mwa m'tseri kumadalitsidwa ndi Mulungu.

Mateyu 6:5:

> Ndipo pamene mupemphera, musakhale monga onyengawo; chifukwa iwo akonda kuimirira ndi kupemphera m'masunagoge ndi pa mphambano za makwalala, kuti aonekere kwa anthu. Indetu ndinena kwa inu, iwo alandiriratu mphotho zawo.

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi sitiyenera kuchita chiyani mmalo moti anthu atione?

________________________________________

==========================================================================

7. Sitiyenera kupemphera pemphero lakuti anthu atiyamikire. Sitiyenera kupemphera pemphero lalitali komanso mokweza kuti anthu aziganiza kuti ife ndiye Akhristu abwino ayi. Imeneyi sinjira yabwino popemphera. Pali njira ina yabwino.

Mateyu 6:6:

> Koma iwe popemphera, loŵa m'chipinda chako, nutseke chitseko chako, nupemphere Atate wako ali m'tseri, ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe.

Kodi n'chifukwa chiyani kupemphera mwa m'tseri kuli kwabwino?

__________________________________________________

==========================================================================

8. Tidzakambirana za izi tonse pamodzi. Izi zimatithandiza kupemphera m'choonadi. Zimatithandiza kuti tisamapemphere modzionetsera kwa anthu. Kodi izi zikutanthauza kuti popemphera tizitsekedwa m'chipinda? Ayi, sizikutanthauza choncho. Zikutanthauza kuti paliponse pomwe mungathe kupemphera mumtima, chifukwa palibe munthu wina angakumveni. Mukhoza kupemphera pamodzi ndi abale ndi alongo pofuna kuwalimbikitsa. Mungathe kupemphera pamodzi ndi anthu ena ndi kubweretsa ulemerero kwa Mulungu. Koma sitiyenera kupemphera mapemphero a akulu kapena mokweza kuti anthu aziganizira kuti ndife a akulu ayi.

Kodi Mulungu adzadalitsa kupereka ndi mapemphero otani? ____________

==========================================================================

Iye adzapereka mphotho kwa zochitika mwa m'tseri.

Mateyu 6:16:

> Ndipo pamene ponse musala kudya, musakhale ndi nkhope yachisoni, ngati onyengawo; pakuti aipitsa nkhope zawo, kuti aonekere kwa anthu kuti ali mkusala kudya. Indetu, ndinena kwa inu alandiriratu mphotho zawo.

Pambali pa kupereka ndi kupemphera, kodi china ndi chiyani chomwe tiyenera kuchita mwa m'tseri? ______________________________

==========================================================

10. Tiyenera kusala mwa m'tseri. Pamene ife tikusala sitiyenera kuuza anthu ena. "Cholinga cha kusala sindicho" kudzionetsera kwa anthu ena kuti ife ndiye Akhristu enieni. Cholinga cha kusala ndi kuonetsa Mulungu kuti tikusowa chinthu china.

Mateyu 6:17-18:

> Koma iwe posala kudya, dzola mutu wako, ndi kusamba nkhope yako.

Kuchokera pa Mateyu 6, kodi ndi kupereka, kupemphera, ndi kusala kotani kumene Mulungu amadalitsa? ______________________________

==========================================================

11. Mulungu amapereka mphotho kwa opereka, kupemphera, ndi kusala mwa m'tseri. Iye sapereka mphotho ngati izi zichitika modzionetsera kwa anthu ena. Yesu anaphunzitsa zinthu zambiri za pemphero. Iye anapatsa ophunzira ake pemphero kuti apemphere. Mukhoza kuphunzira za pempheroli m'buku lotchedwa <u>Kulankhula ndi Mulungu</u>.

Tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu mutu 6:1 mpaka 15. Kuchokera pa ndime 14, kodi tiyenera kuchita chiyani kwa anthu amene atichimwira? ______________________________

==========================================================

12. Tiyenera kuwakhululukira. Zoona, ngati anthu atichimwira tiyenera kunena kuti, "ndakukhululukirani." Ndipo tiyenera kuwakhululukiradi

kuchokera pansi pa mitima yathu. Koma izi sizimene anthu a dziko lapansi amachita. Sizimenenso ife timachita mwa ife tokha. Koma tikhoza kukhululukira ngati ife tikhulupirira Mulungu ndi kumupempha kuti atithandize. Ngati sitikhululukira ena, ifenso sitidzakhululukidwa.

Mateyu 6:14:

> Pakuti ngati mukhululukira anthu zolakwa zawo adzakhululukira inunso Atate wanu wa kumwamba.

Kodi ndani amene sadzakhululukira zolakwa zathu ngati ife sitikhululukira ena?

________________________________________

==========================================================================

13. Mulungu sadzatikhululukira. Iye sadzamva ngakhale mapemphero athu. Mwinatu mapemphero anu sayankhidwa. Kapena ndi chifukwa chakuti simunakhululukire munthu wina kuchokera pansi pa mtima wanu. Ichi ndi chimene tiyenera kupempherera.

Mateyu 6:12:

> Ndipo mutikhululukire mangaŵa athu, monga ifenso takhululukira a mangaŵa athu.

Taganizira za moyo wanu. Kodi pali munthu wina amene wakuchimwirani sabata lino?

____________________________

==========================================================================

14. Taganizirani zimene munachita pamene munthu wina anakuchimwirani Takumbukirani zimene munanena. Kumbukirani zimene munaganiza. Ganizirani mmene mukumvera tsopano mumtima mwanu pa zimenezi.

Kodi munakhululukira zimene munthu ameneyu anachita? ____________

Kodi chidzachitika n'chiyani ngati sitikhululukira anthu amene atichimwira?

________________________________________

==========================================================================

15. Mulungu sadzatikhululukira. Nthaŵi zina Yesu anauza anthu za akapolo aŵiri. Kapolo woyambayu akakongola ndalama zambiri kwa mfumu. Iye anadandaula kwa mfumu ndipo mfumuyo inamukhululukira mangaŵa ake. Ndipo

munthu ameneyu anapita kukalonjerera ngongole kwa kapolo wina amene anamukongoza ndalama zochepa kuti amubwezere. Ndipo poona kuti mnzakeyo sanathe kubweza ndalamazo anamugwira namukanyanga pakhosi ndi kumponya m'ndende.

Mateyu 18:32-33:

> Pomwepo mbuye wake anamuitana iye, nanena naye, kapolo iwe woipa, ndinakukhululukira iwe mangaŵa onse aja momwe muja unandipempha ine; kodi iwenso sukadamchitira kapolo mnzako chisoni, monga inenso ndinakuchitira iwe chisoni?

Kodi tiyenera kuchita chiyani ngati anthu atichimwira?

---

16. Tiyenera kuwakhululukira. Palibe mmodzi amene amakhala wolungama pa moyo wake wonse. Ife tonse tinachimwa ndipo tisoŵa chikhululukiro. Tifunika kutsukidwa ndi mwazi wa Yesu kuti machimo athu achotsedwe. Koma kapolo uja anamangitsa mbale wake chifukwa cha ndalama zochepa. Pamene mfumu ija inamva inakwiya kwambiri. Iyo inamugwira kapoloyo ndi kumuponyanso m'ndende kufikira atabweza ndalamazo.

Mateyu 18:35:

> Chomwechonso Atate wanga adzachitira inu, ngati inu simukhululukira yense mbale wake ndi mitima yanu.

Kodi chidzachitike n'chiyani ngati sitikhululukira anthu ena omwe atichimwira?

---

17. Mulungu sadzatikhululukira. Choncho tikuona kuti kusakhululukira kumabweretsa mavuto. Zimatsekereza kuti tisakhululukidwe. Miyoyo yathu imakhala yofooka ndipo timagonjetsedwa. Komanso zimabweretsa mavuto mumpingo.

Tunde anali mbusa wochepa. Bambo wina wachikulire mumpingo anauza abwenzi ake kuti Tunde ndi wochepa. Iye anati Tunde afunika nzeru zambiri asanayambe kulalikira. Ndipo Tunde atamva zimene bambo ameneyu anali kunena, anakwiya. Iye sanafune kulankhula naye bambo ameneyu. Iye anakana kumukhululukira. Ndipo anthu amumpingomo anatsatira zimene anali kunena anthu aŵiriŵa. Ena anali kuvomereza za zimene bamboyu anali kunena. Ena anali kuvomereza zimene mbusa wochepayu anali kunena. Ndipo mpingo unataya nthaŵi yake kungokangana mmalo mobweretsa anthu kwa

Yesu.

Kodi mmodzi mwa anthu amenewa mukadakhala inu? Khalani ndi nthawi tsopano yodzifufuza mwa inu nokha. Mpempheni Mulungu kuti akuonetseni mtima wanu. Kodi ndi zoona kuti munakhululukira onse amene anakuchimwirani?

____________________________________________

==========================================================================

18. Kuchokera pa Mateyu 6, kodi ndi kupereka, kupemphera, ndi kusala kotani kumene Mulungu adzapereke mphotho?

__________ __ __ __________

============================

Kodi chidzachitika n'chiyani ngati sitikhululukira anthu amene atichimwira?

__________________________________________________________

==========================================================================

SABATA LACHISANU NDI CHITATU: KHRISTU APHUNZITSA ZINA ZAMBIRI PA PHIRI
TSIKU LOYAMBA: SITINGATHE KUTUMIKIRA MULUNGU NDI CHUMA

1. Lero tili kuyamba kuyamba kuphunzira zina za chiphunzitso cha Yesu cha pa phiri. Tiyenera kuphunzira zinthu zonsezi bwino.

Kuchokera pa Mateyu 6, kodi ndi maperekedwe a mtundu wanji, mapempheredwe ndi masalidwe wotani amene Mulungu amapereka mphotho?

______________

Kodi chingaoneke ndi chiyani ngati ife sitikhululukira anthu ena amene amatilakwira ife?

______________________________________________

==============================================================

2. Mulungu amapereka mphotho kwa opereka, opemphera ndi osala amene amachita mwa m'tseri. Ngati ife sitikhululukira anthu ena, Mulungu sadzatikhulukukira.

Lero tili ndi phunziro lalikulu pa chuma. Anthu amasiku a Yesu anali kuyesedwa kuti azikonda ndalama ndi zinthu. Yesu anachenjeza ophunzira za zimenezi.

(1) Ngati titayesa kutumikira Mulungu ndi chuma, tidzadana ndi Mulungu ndi kukonda zinthu za dziko lapansi.

(2) Mateyu 6:33 amati: koma muthange mwafuna ufumu wake ndi chilungamo chake, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 6:24 mpaka 33. Kodi muli kuganiza kuti anthu ambiri lero amafunafuna ndalama ndi chuma?

--------------------------------------------------------------

______________________________________________________________

==============================================================

3. Ine ndili kuganizira kuti anthu ambiri amakhala ali kufunafuna ndalama. Kwa iwo zimenezo ndi zofunika kwambiri koposa kumvera Mulungu Ife timaona zimene potizungulira.

Timaonanso zinthu za dziko lapansi. Ife timafuna chakudya ndi nyumba zabwino. Ife timafuna zovala zabwino ndi ndalama zambiri. Timafuna maphunziro a ana athu ndi magalimoto okweramo. Zinthu zimenezi sizoipa ayi. Koma zimenezi siziyenera kukhala zoyamba m'miyoyo yathu.

Mateyu 6:32:

Pakuti anthu akunja azifunitsa zonse zimenezo; pakuti Atate wanu wa kumwamba adziŵa kuti musoŵa zonse zimenezo.

Kodi ndi zinthu zotani zimene Mulungu amazidziŵa kuti ife timazisoŵa?

---

============================================================

4. Mulungu amadziŵa kuti ife timafuna zinthu za dziko lapansi. Iye amadziŵa kuti ife timasoŵa zakudya ndi zovala ndi nyumba. Timaona anthu amene ali potizungulira ali kupeza zinthu zabwino. Yesu ananena kuti amitundu anali kufuna zinthu zimenezi. Amitundu anali amene sanadziŵe Mulungu pa nthaŵi imeneyo. Iwo anaika ndalama ndi zinthu zina kukhala zoyamba m'miyoyo yawo.

Mateyu 6:24:

Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa Ambuye aŵiri: pakuti pena adzamuda mmodziyo, ndi kukonda winayo; pena adzakangamira kwa mmodzi, nadzanyoza wina. Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa chuma.

Kodi ife tikhoza kukhala tikufunafuna zinthu za dziko ndi kutumikira Mulungu?

---

============================================================

5. Ife sitingathe kutumikira onse aŵiri. Ngati poyamba tikufuna zinthu za dziko lapansi, izo zimakhala mbuye wathu. Zimalamulira miyoyo yathu. Tikhoza kumangoganiza za kupeza zinthu zina zambiri. Ngati tiyesetsa kukhala ndi moyo wokondweretsa Mulungu timakhala m'mavuto. Ndi zofanana ngati munthu wofuna kugwirira ntchito anthu aŵiri osiyana pa nthaŵi imodzi. Pamene tikugwirira ntchito wina, winanso atiuza ife kuchitanso kanthu kena. Ife sitingathe kugwira ntchito motere. Ife tiyenera kusankha pakati pa Ambuye aŵiri.

Kodi inu munayesapo kugwirira ntchito anthu aŵiri pa nthaŵi imodzi?

---

Kodi chingaoneke ndi chiyani ngati mutayesa kuchita zimenezi?

==========================================================================

6. Tidzakambirana za zimenezo tonse pamodzi. Ngati mutayesa kugwirira ntchito anthu aŵiri, ndiye kuti mumamvera mmodzi ndi kudana ndi winayo. Inu simungathe kukhala olamulidwa ndi onsewo pa nthaŵi imodzi. Chimenechi ndi chimodzimodzi ndi chuma ndi Mulungu.

Mateyu 6:24:
Pakuti pena adzamuda mmodziyo, ndi kukonda winayo.

Kodi ndi chiyani chimene chimachitika ngati tikuyesa kutumikira Mulungu ndi chuma cha m'dziko lapansi pa nthaŵi imodzi?

==========================================================================

7. Ndiye kuti tidzadana ndi Mulungu ndi kukonda zinthu za dziko lapansi. Ngati tikondadi Mulungu moona, ndiye kuti zofuna za chuma sizidzakhala zofunika kwambiri. Sitidzayesa kupeza zina ndi zina. Koma ngati tikonda chuma, ndiye kuti tidzaiwala Mulungu. Iye sadzaoneka ngati wofunika kwambiri. Nthaŵi yathu yonse idzatayika tikuganizira kuti tipeze zinthu zina zoonjezera za pa dziko lapansi.

Mateyu 6:33:
Koma muthange mwafuna Ufumu wake ndi chilungamo chake, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu.

Ganizirani za ndime imeneyi. Nanga ife timatumikira Mulungu, kodi ndi ndani amene adzatipatsa zinthu za dziko zomwe tidzazifuna?

==========================================================================

8. Mulungu adzaona kuti ife tazipeza izo. Tidzagwira ntcniyoyo bwino. Tidzapeza chakudya ndi zovala. Koma zimenezo sizidzakhala zinthu zazikulu m'miyoyo yathu. Ife sitidzalakalaka kukhala ndi chuma choposa. Tidzakhala wodera nkhaŵa kwambiri za ntchito yomwe tikugwirira Mulungu. Tidzakhala wodera nkhaŵa za mmene ife tingamukondere Iye.

Mateyu 6:30-31:

Koma ngati Mulungu aveka chotero maudzu a kuthengo, akhala lero, ndi maŵa aponyedwa pamoto, nanga si inu kopambana ndithu, inu akukhulupirira pang'ono? Chifukwa chake musadere nkhaŵa, ndi kuti tidzadya chiyani? Kapena Tidzamwa chiyani? Kapena tidzavala chiyani?

Kodi ndi chiyani chongaoneke ngati tiyesa kutumikira Mulungu ndi zinthu za dziko lapansi pa nthaŵi imodzi?

____________________________________

____________________________________________________________________.

============================================================

9. Ife tidzadana ndi Mulungu ndi kukonda zinthu za dziko lapansi. Yang'ananinso zimene Yesu ananena.

Mateyu 6:33:

Koma muthange mwafuna ufumu wake ndi chilungamo chake, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu.

M'ndime imeneyi, kodi Yesu anati poyamba tiyenera kuika chiyani m'miyoyo yathu?

_________________________________________________________

============================================================

10. Poyamba tiyenera kufuna ufumu wa Mulungu ndi chilungamo chake. Tiyenera kumvera Mulungu koposa ndalama. Kutenga nthaŵi ya mapemphero ndi kuphunzira Buku Lopatulika mwina kukhoza kumatilandiritsa ndalama zochepa. Koma ife tiyenera kugaŵira ena. Kupatsa anthu muyeso wodzala mnyumba yosungiramo kumatanthauza kukhala ndi phindu lochepa. Koma ife tiyenera kumapereka muyeso wodzala.

Audu ndi wosoka zovala (kapena kuti telala). Iye amagwirira ntchito munthu amene sali Mkhristu. Anthu amabwera kudzagula zovala. Mwini sitoloyo amauza anthu kuti nsaluzo ndi zolimba koma pamene sizolimba. Iye amauza anthu kuti ndi zopangidwa ku thonje lodula lapamwamba koma pomwe siziri chomwecho. Audu safuna kumanena zonama za nsaruzo. Koma mwini sitolo anati ngati Audu safuna kumanyengeza anthu, adzamuchotsa ntchito.

Ngati Audu poyamba akadafuna ufumu wa Mulungu ndi chilungamo chake, kodi iye adzachita chiyani?

_________________________________________

11. Audu akhoza kusiya ntchito imeneyi. Zimenezi mwina zikhoza kukhala zovuta kwambiri. Mwina zikhoza kukhala zovuta kupeza ntchito ina. Audu akhoza kulankhula kwa mwini sitolo. Iye akhoza kuyesa kumuonetsa iye kuti ndi bwino kunena zoona. Koma ngati mwini akana, Audu akhoza kusiya ntchito.

Dupe anali ndi malo amunda wake abwino. Zinthu zonse zimene iye anali kubzala zinali kukula bwino. Ndipo iye anayamba kuzigulitsa. Koma mbale wake woyandikana naye anagula galimoto yaikulu ya lole ndipo anayamba kumatengera mbewu zaziŵisi za Dupe kupita nazo ku tauni. Iwo anali kubweretsa ndalama zambiri. Dupe anali kukondweretsedwa. Iye anali kubzala zinthu zambiri m'munda mwake. Ndipo anali kugwira ntchito ya m'munda mwake mmalo mopita ku tchalitchi.

Ngati Dupe akadafuna Mulungu poyamba, kodi iye akadachita chiyani? Kodi iye akadamagwira ntchito pa nthaŵi yopita ku tchalitchi kapena akadamapita kukapemphera ku tchalitchi?

________________________________________

________________________________________________________________________

========================================================================

12. Dupe akhoza kupita ku tchalitchi. Iye sayenera kulola kuti munda wake utenge nthaŵi imene ili ya Mulungu. Dupe mwina akhoza kumapeza ndalama zochepa ngati iye azimupatulira Mulungu nthaŵi. Koma iye sangathe kutumikira ndalama ndi Mulungu. Zimenezi ndizo zimatanthauza kufuna Mulungu poyamba.

Mateyu 6:33:

> Koma muthange mwafuna ufumu wake ndi chilungamo chake ndipo zonse zimenezo zidzanjezedwa kwa inu.

Tsopano yambani mwaima ndi kuloŵeza ndime imeneyi. Ngati munganene mosaonera, ilembeni apa.

______________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

========================================================================

13. Imeneyi ndi ndime yofunika koposa ku miyoyo yathu. Idzatithandiza ife kukhala ndi maganizo ambiri. Nthaŵi zina ife sitidziŵa zoyenera kuchita. Sitidziŵa ngati tiri oyenera kugwirira ntchito Mulungu kapena kudzigwirira tokha. Nthaŵi zina sitidziŵa ngati tiyenera kulalikira

kapena kusamalira mabanja athu. Mulungu adzatithandiza kuti tikhale ndi maganizowo. Iye adzationetsa ife mmene tingachitire ntchito yathu bwino ndi kuti timufune Iye poyamba.

Nenani nokha Mateyu 6:33. Ngati ife titumikira Mulungu mokhulupirika ndikukhala ndi miyoyo yolungama, kodi chidzaoneka ndi chiyani pa zinthu zimene timazisoŵa?

________________________________________________________

________________________________________________________________________

==========================================================================

14. Zinthu zimenezi zidzakhalanso zathu. Zimenezi sizikutanthauza kuti tidzakhala ndi zinthu zonse zimene timazifuna. Zimatanthauza kuti tidzakhala ndi zokwanira pokhala ndi moyo. Sizimatanthauza kuti tidzakhala olemera mu zinthu za dziko lapansi. Chimatanthauza kuti Mulungu adzatipatsa zomwe tiyenera kukhala nazo.

Kodi chimaoneka ndi chiyani ngati tiri kufuna kutumikira Mulungu ndi zinthu za dziko lapansi?

__________________________________________________

________________________________________________________________________

==========================================================================

15. Tidzadana ndi Mulungu ndi kukonda zinthu za dziko lapansi.

Kodi ndi ndime iti imene imatiuza choyenera kufuna poyamba. Lembani kumene imapezeka ndipo munene nokha mawu a ndimeyo.

______________________

________________________________________________________________________

==========================================================================

16. Ndime imeneyi ndi Mateyu 6:33: Anthu ambiri ali ndi mavuto chifukwa iwo sakhulupirira ndime imeneyi. Iwo saitsata ndimeyi. Iwo saika Mulungu kukhala m'miyoyo yawo. Iwo saika chilungamo patsogolo pa chuma chawo.

Anthu anu asoŵa kumvetsetsa phunziro limeneli. Konzani ulaliki kuchokera'm'ndime zimenezi papepala lina lembani zinthu zazikuluzikulu zimene